SABATA LACHINAYI: KODI TIYENERA KUPEMPHERERA CHIYANI?
TSIKU LOYAMBA:

Sabata latha tinaphunzira za nthaŵi zimene tiyenera kupemphera. Mwina mwake mumaganiza kuti, "Pali nthaŵi zambiri zimene tiyenera kupemphera. Zikuoneka kuti tiyenera kumangopemphera pafupifupi nthaŵi iliyonse." Inde, ndimo mmene ziyenera kukhalira. Kodi mukukumbukira ndime imene tinawerenga.

1 Atesalonika 5:17:
Pempherani kosalekeza.

Tsopano muli kuganizira, "Koma ndiyenera kupempherera chiyani nthaŵi zonse. Zinthu zimene ndidzazipempherera zidzatha posachedwa, nanga ndidzanena chiyani?" Zimenezi ndi zimene tikufuna kulankhula sabata ino. Ndiyembekeza kuti pamene tizitha phunziroli simudzafunsa zimene mudzazipempherera.

1. Kodi mungathe kulemba nthaŵi imene tiyenera kupemphera? Ngati mufuna, onaninso ku phunziro la sabata latha musanalembe, koma musaonere ayi.

   (1) ____________________

   (2) ____________________

   (3) ____________________

   (4) ____________________

==========================================================

Tsopano nanga tidzapempherera pa nthaŵi zonsezi?
Ngati kupemphera kuli kulankhula ndi Mulungu ndiye kuti tisamangopempha zinthu zambiri-mbiri. Tiyeni tiyambe mapemphero athu pomutamanda ndi kumuthokoza Iye chifukwa cha chikondi chake.

2. Kodi ndiyambe mapemphero anga pomupempha Mulungu kuti andichiritse?

   ____________________

==========================================================

Koma tiyenera kuthokoza chifukwa ninji? Nthaŵi zina tikamakhala ndi mabvuto ambiri. Izi zimaoneka ngati kuti palibenso chabwino chakuti tingachiganizire. Koma tangoyambani ndi kuganizira zinthu zimene Mulungu wakupatsani. Muthokozeni chifukwa cha chakudya ndi nyumba yogonamo. M'thokozeni chifukwa cha banja lanu. M'thokozeni chifukwa cha ntchito imene muli kugwira.

3. Talembani zina zimene inu m'moyo mwanu muyenera kumuthokozera Mulungu pamene muli kupemphera.

______________________________________________

---

Choncho yambani kuganiza za Mulungu ndikumuthokoza chifukwa cha mmene Iye alili.

4. Pano pali m'ndandanda wa zinthu za momwe Mulungu alili. Ikani chizindikiro ngati ichi + pa zonse zimene zioneka ngati ndizofunika kwambiri kwa inu. Ndipo muyambe kumuthokoza Mulungu pa zinthu zimenezi.

Mulungu ali wamphamvu zonse.
Mulungu ali ponseponse.
Mulungu amadziŵa zonse.
Mulungu amakukondani.
Mulungu ali nanu nthaŵi zonse.
Mulungu sasintha konse.
Mulungu amakhululukira machimo.
Mulungu amakumvetsetsani.
Mulungu amayankha pemphero.
Mulungu ali kukukonzerani malo.

---

5. Kuli bwino kuyamba kupemphera mwa ______________

---

Mulungu amatikonda ndipo Iye amafunanso chikondi chathu. Pamene tiyamba kupemphera mwa kum'thokoza Iye chifukwa cha momwe alili, ndiye kuti tikusonyeza chikondi chathu kwa Iye. Mitima yathu imakhala yachikondi. Kotero timakhala okonzekera kupempherera zinthu zina.

Kodi tingayambe bwanji kupemphera?

______________________

______________________________________________

=======================================================

*******************************************************

MAYANKHO

5. Kuthokoza Mulungu.
3. Chingathe kukhala chilichonse monga mvula, abwenzi, umoyo wabwino.
1. Onani ku Sabata la 3 Tsiku la 5.
6. Tiyenera kuyamba kupemphera mwa kuthokoza Mulungu.
2. Ayi, tiyenera kuyamba ndikumutamanda.
4. Inu mukudziŵa zimene zili zofunika kwa inu.

SABATA LACHINAYI: KODI TIYENERA KUPEMPHERERA CHIYANI?
TSIKU LACHIŴIRI:

Taphunzira kuti kupemphera sikungopempha zinthu kokha ayi. Kupemphera ndiko kulankhula ndi Mulungu monga mmene tingalankhulire ndi bwenzi lathu.

1. Kodi tingayambe bwanji kupemphera? ____________________

______________________________________________

==========================================================

Tikatha kuthokoza, nanga tiyenera kupemphera motani? Pakuti Mulungu ndi Bwenzi lathu ndipo Atate wathu alinso ndi chidwi pa zosoŵa zathu. Pali zosoŵa zambiri zimene tiyenera kuzipempherera mwakuti nkobvuta kudziŵa pemphero limene tingayambe kupemphera nalo.

2. Kodi ndizosoŵa zandani zimene mumazidziŵa kwambiri?

______________________________________________

Nanga ndani amene mumampempherera poyamba?

______________________________________________

==========================================================

Kodi mwa inu nokha mungapempherere chiyani? Tingathe kulemba zinthu zambirimbiri. Pali zinthu monga chakudya, zovala ndalama ndi kupambana pa ntchito yanu. Kodi mukumbukira zimene Yesu anauza ophunzira ake kuti apemphe pamene anali kuŵaphunzitsa kupemphera? Iye anaŵauza kuti azinena kuti:

Mateyu 6:11:
Mutipatse ife lero chakudya chathu cha lero.

3. Kodi ndi choyenera kwa ife kumampempha Mulungu kuti atithandize pa zosoŵa zathu za tsiku ndi tsiku?

Inde, Mulungu ali ndi chidwi ndi zinthu zimenezi ndipo amafuna kutithandiza. Koma tiyenera kutenga nthaŵi yaitali pang'ono tikupempherera zinthu zimenezi. Yesu anauzanso ophunzira ake pa mutu wokhawokhawu,

Mateyu 6:25:
> Chifukwa chake ndinena kwa inu, musadere nkhaŵa kapena thupi lanu, chimene mudzavala. Kodi moyo siuli woposa chakudya, ndi thupi loposa chovala?

4. Kodi Yesu anatanthauzanji pamene anati, "Indetu moyo umaposa chakudya, thupi limaposa zovala?

___

___

==========

Yesu anapitiriza ndi kunena kuti,

Mateyu 6:33:
> Koma muyambe mwafuna ufumu wake wa Mulungu ndi chilungamo chake, ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwa inu.

Izi zimatithandiza ife kuona zimene tiyenera kumadzipempherera mwa ife tokha.

5. Ngati tikuganizira za ufumu wa Mulungu ndi chilungamo chake tisanaganize chilichonse, kodi ndi zinthu zotani zimene tikanadzipempherera mwa ife tokha?

___

==========

Munthu amene amafunitsitsadi ufumu wa Mulungu ayenera kudziŵa njira ya Mulungu. Iye adzapemphera kuti amvetsetse bwino Mawu a Mulungu ndipo kuti adzapempherera mphamvu yakuti aŵamvere Mawuwo. Ngati iye ali kupempherera Ufumu wa Mulungu ndiye kuti adzapempha mphamvu ndi nzeru zochitira ntchito ya Mulungu.

6. Kodi mumakhala muli kupempherera zinthu zimenezi mwa inu nokha?

______________________________

==========================================================

Kupemphera kwakuti munthu amvetsetsa ndikukhala ndi mphamvu kuli kofunika kwambiri kuposa kupempherera chakudya ndi zovala ndi zinthu zina zake zotikondweretsa. Mulungu amalonjeza kutimvera ife pamene tipempha zinthu zofunika kwambiri.

Yakobo 1:5:
> Ngati wina wa inu ikamusoŵa nzeru, apemphe kwa Mulungu, amene apatsa kwa onse modzala manja. niwosatonza; ndipo adzampatsa iye.

7. Kodi ife tikuuzidwa kuti tipemphe chiyani m'ndime imeneyi?

______________________________

==========================================================

Choncho tiyeni tisamangopempherera zinthu zongosangalatsa miyoyo yathu. Tiyeni tipemphere kuti tikhale monga momwe Mulungu akutifunira kuti ndimo mmene tizikhalira. Tiyeni tipemphere kuti tikhale ndi nzeru, mphamvu, ndi chikondi m'moyo mwathu. Paulo anati chinthu chachikulu chimene iye anali kufuna m'moyo mwake chinali kukhala ndi chilungamo cha Mulungu ndiponso kumudziŵa Khristu.

Afilipi 3:10:
> Kuti ndimzindikire Iye, ndi mphamvu yakuuka kwake, ndi chiyanjano cha zoŵaŵa zake, pofanizidwa ndi imfa yake.

8. Onaninso mwa kulibwereza phunziroli ndipo mulembe zinthu zimene tiyenera kudzipempherera mwa ife tokha.

______________________________

______________________________

______________________________

==========================================================

***********************************************************

MAYANKHO.

1. Pakuthokoza Mulungu.
5. Tidzakambirana za zimenezi m'kalasi.
4. Mukanayenera kulemba motere: Pali zofunika zambiri zoposa zakudya kapena zovala.
7. Nzeru.
3. Inde.
6. Ndiganiza kuti mumapempherera zinthu zimenezi. Ngati simutero yambani kuzipempherera tsopano.
2. Timadzipempherera tokha poyamba chifukwa timadziŵa bwino zosoŵa zathu.
8. Chakudya, zovala, ndalama, kupambana pa ntchito yathu mphamvu zomvera Mulungu, nzeru, ndi chikondi.

## SABATA LACHINAYI: KODI TIYENERA KUPEMPHERERA CHIYANI?
## TSIKU LACHITATU:

Dzulo tinaphunzira kuti chimodzi cha zinthu zazikuluzikulu zimene timafunira kupemphera ndi kumadzipempherera mwa ife tokha. Tinaphunziranso kuti tisamangopempherera zinthu monga chakudya, ndi zovala, ndi chisangalalo cha ife tokha ayi.

1. Kodi zinthu zofunika kwambiri ndi ziti zimene tiyenera kumazipempherera mwa ife tokha?

Muzidzipempherera nokha kwambiri. Komanso pamene muli kudzipempherera, musaiŵalenso anthu ena. Kodi mumadziŵa kuti kungakhale kotheka kukhala waumbombo ngakhale ndi m'mapemphero momwe? Ife sitikonda munthu amene amafuna ndi kusunga zonse mwa iye yekha. Pemphero ndi chinthu chimene tingathe kugwiritsa ntchito pakuthandiza anzathu kuŵapempherera.

2. Ngati sindipempherera anthu ena, kodi ine ndine munthu wotani?

Yambani kupempherera apabanja lanu. Ngati muli wokwatira pemphererani mkazi kapena mwamuna wanu. Mpempheni Mulungu kuti ampatse zinthu zabwino m'moyo mwake monga zinthu za thupi ndi zinthu za uzimu monga momwe inu mumadzipempherera. (Pamene muli kumupempherera, dzipemphererenso kuti mukhale bambo wabwino kapena mayi wabwino). Ngati muli ndi ana, kumbukirani kuti ndinu amene munaŵabweretsa m'dziko lino. Muli ndi udindo waukulu woŵasonyeza njira yabwino m'miyoyo mwawo. Apemphereni ana anu tsiku lililonse. Ndipo musaiŵale kumupempha Mulungu kuti akupangeni kukhala kholo labwino.

3. Mungathe kuthandiza mkazi wanu ndi ana anu tsiku lililonse paku

______________________________________________

==========================================================

Pempherani makolo anu. Muthokozeni Mulungu chifukwa cha iwo Simungazindikire mpaka mutakalamba monga mmene iwo alili tsopano ndi kuzindikira kuti akupatsani zinthu zambiri ndiponso akuchitirani zinthu zambiri. Mpempheni Mulungu zimene mungathe kuŵachitira. Apempherereni abale ndi alongo anu, ang'ono awo a mayi anu, azakhali anu, ndi achibale ena amene ali ndi zofuna zapadera. Ena alikudwala. Ena ali ndi mabvuto. Ena alikukana kumutsatira Mulungu. Makamaka apempherereni ameneŵa.

4. Popeza sikutheka kuti muzipempherera abale anu onse nthaŵi ndi nthaŵi, nanga ena ndani amene mukhoza kuŵapempherera?

______________________________________________

==========================================================

Achinansi anu apempherereninso. Ambiri a iwo sapita ku tchalitchi kapena kuwerenga Buku Lopatulika. Iwo sapemphera. Njira yokhayo imene amamzindikira Mulungu ndi zimene iwo amaona mwa inu. Kodi mukukumbukira zimene Yesu ananena za kuunika kwa dziko lapansi?

Yohane 8:12:
"Ine ndine kuunika kwa dziko lapansi."

Komanso nthaŵi ina ananenanso mawu aŵa:
Mateyu 5:14:
"Inu ndinu kuunika kwa dziko lapansi."

Iye ananenanso kuti:
Mateyu 5:13:
"Inu ndinu mchere wa dziko lapansi."

Pamene tikonda anzathu ndi kuŵapempherera, tikhala ngati kuunika ndi mchere kwa iwo. Taganizirani za mmene mchere umasinthira chakudya chathu ngati chinali choipa kuti chikhale chabwino. Taganizirani mmene mapemphero anu

amasinthira anansi anu oipa kuti akhale abwino.

5. Kodi mungaŵasinthe anzanu oipa kuti akhale abwino?

_______________ Nanga mungazichite bwanji zimenezi?

==========================================================

Ndiponso ndikosatheka kupempherera anansi anu onse nthaŵi zonse. Nanga mungaŵapempherere bwanji? Njira imodzi ndiyo yopempherera gulu lina masiku ena. Mukhoza kupempherera gulu limene lili cha ku mmaŵa pa tsiku lolemba. Ndi ena amene ali cha kum'mwera pa tsiku lachiŵiri. Ndi ena amene ali cha kuzambwe (kumadzulo) pa tsiku lachitatu. Komanso ena amene ali cha kumpoto pa tsiku lachinayi.

6. Kodi munayamba mwaganizirapo zoŵapempherera anzanuŵa motere?

_______________

==========================================================

Njira ina ndiyo kusankha mmodzi kapena aŵiri kapena atatu kuti muziŵapempherera pa nthaŵi yake tsiku lililonse. Mpempheni Mulungu kuti akulangizeni amene mungaŵapempherere. Ganizirani zosoŵa zawo ndi mphamvu zawo zimene angathe kutsogolera nazo anthu ena oŵazungulira. Mumvereni Mulungu kuti akupatseni ena omwe muyenera kuchita nawo chidwi mumtima mwanu. Mwa ichi muziŵapempherera masiku onse kuti adzakhale Akhristu.

7. Kodi mungasankhe bwanji anansi amene mungathe kuŵapempherera?

_______________________________________________

_______________________________________________

==========================================================

Inu mukuyesa kuti iyi ndi ntchito yaikulu kwambiri. Komatu sizokhazi zozipempherera ayi. Werengani ndime iyi kuchokera pa 1 Timoteo 2:1-2:

1 Timoteo 2:1-2:

> Ndidandaulira tsono, poyambayamba kuti achitike mapembedzo, mapemphero, mapembadzero, mayamiko, chifukwa cha anthu onse; chifukwa cha mafumu ndi onse akuchita ulamuliri; kuti m'moyo mwathu tikakhale odekha mtima ndi achete mkulemekeza Mulungu, ndi mkulemekezeka monse.

8. Kodi ndime imeneyi akutiuza kuti tizipempherera ndani?

______________________________________________

==================================================

Ntchito yathu ya mapemphero imafikira ku mabanja athu ndi kwa anzathu ena. Pa ndime iyi akutiuza kuti tipempherere anthu onse, makamaka kwa iwo amene ali otilamulira.

9. Kodi timpempherere Purezident?

____________________

==================================================

Atsogoleri athu akuyesetsa kutithandiza. Ndi chinthu chabwino kuti tiziŵapempherera pa ntchito yawo. Koma pali anthu ena amene sayesa kutithandiza. Aŵa ndiwo adani athu. Ngakhale ameneŵanso, Mulungu amatiuza kuti tiziŵapempherera.

Mateyu 5:44:

> Koma ine ndinena kwa inu kondanani nawo adani anu, ndikupempherera iwo akuzunza inu.

Mwina ameneŵa ndi ena mwa ovutitsitsa kuwapempherera koma ndi zimene Mulungu akutiuza ife kuti tizichita.

10. Kuonjezapo kukonda adani athu, kodi tiziŵapangira chiyani?

________________________________________

==================================================

Pali zinthu zambiri zimene tiyenera kuzipempherera.

11. Ganiziraninso za phunziro ili ndipo mulembe anthu onse amene tiyenera kuŵapempherera.

______________ ______________ ______________

______________ ______________ ______________

______________ ______________ ______________

==========================================================

**********************************************************

MAYANKHO.

8. Anthu onse, makamaka olamulira.
5. Inde, pakupemphera.
2. Munthu waumbombo.
11. Mungathe kupeza nokha mayankho ake mphunziroli.
9. Inde.
6. Mudziyankhire nokha.
3. Muŵapempherere.
1. Kudziŵa njira ya Mulungu ndi kumvera Iye, kukhala anzeru, amphamvu ndi achikondi.
10. Tiyenera kuŵapempherera.
7. Mumupemphe Mulungu kuti akulangizeni.
4. Iwo amene Mulungu aŵaika m'maganizo anu chifukwa ali ndi zosoŵa zapadera.

SABATA LACHINAYI: KODI TIYENERA KUPEMPHERERA CHIYANI?
TSIKU LACHINAYI:

Pakali pano taphunzira zinthu zambiri zimene tiyenera kupempherera. Koma sitiyenera kuyamba mapemphero athu ndi kupempha zinthu ayi.

1. Kodi tingayambe bwanji mapemphero athu? ______________

______________________________________________________

==========================================================

Tikatha kumlemekeza Mulungu tiyamba kuganiza mmene angatithandizire. Tidzipempherere ife tokha pa zinthu zimene tikuzisoŵa. Nkosabvuta kudzipempherera koma ngati sitikhala a umbombo ndi mapemphero athu ndiye kuti tidzapemphereranso anthu ena.

2. Mosaonera, lembani anthu ena onse amene tiyenera kuŵapempherera.

______________ ______________ ______________

______________ ______________ ______________

==========================================================

Tiyeni tione m'Buku Lopatulika kuti tipeze gulu lina la anthu oyenera kupemphereredwa. Werengani ndime izi mosamalitsa ndipo muone kuti ndi mtundu uti wa anthu umene ukusoŵa mapemphero athu.

Aefero 6:18:
Mwa pemphero lonse, ndi pembedzero, mupemphere nthaŵi yonse mwa Mzimu, ndipo pochezera pamenepo chichezerere ndi kupembedzera oyera mtima onse

1 Samueli 12:23:
Ndipo inenso, kukhala kutali ndi ine, kuchimwira Yehova ndi kuleka kukupemphererani, koma ndidżakulangizani njira yabwino ndi yolungama.

(Izi zinanenedwa ndi Samueli kuuza ana a Israyeli)

Afilipi 1:3-4:
Ndiyamika Mulungu wanga pokumbukira inu ponse; nthaŵi zonse m'pembedzero langa lonse la kwa inu nonse ndichita pembedzerolo ndi kukondwera.

Akolose 4:2-3:
Chitani khama mkupemphera, nimudikire momwemo ndi chiyamiko ndikutipempherera ifenso pomwepo, kuti Mulungu atitsegulire ife pakhomo pa mawu, kuti tilankhule chinsinsi cha Khristu, chimenenso ndikhalira m'ndende. (Mawu aŵa analembedwa ndi mtumwi Paulo ku mpingo wa kwa Akolose).

Yakobo 5:16:
Chifukwa chake mubvomerezane wina ndi mnzake machimo anu, ndipo mupempherere wina kwa mnzake kuti muchiritsidwe. Pemphero la munthu wolungama likhoza kwakukulu m'machitidwe ake.

3. Kodi ndi anthu a mtundu wanji amene ali kupempherereredwa pa ndime izi?

______________________________

==========================================================

Pano pali mtundu wa anthu umene ife nthaŵi zina timaiŵala kuupempherera. Ndiwo Akhristu amumpingo. Nthaŵi zina timaganizira kuti mpingo siufuna kupempherereredwa. Timaganizira kuti anthu ameneŵa anadzipereka kale kwa Mulungu ndipo ali ndi mphamvu kale.

4. Kodi Buku Lopatulika limanena kuti anthu amumpingo ndi wofunika kuti apempherereredwe?

________________

==========================================================

Inde, Buku Lopatulika limanena zambiri zopempherera Akhristu ena kuposa kupempherera ochimwa. Makamaka akulu ampingo amasoŵa mapemphero athu. Mu Akolose 4:2-3 mmene tawerenga poyamba pa phunziro ili, Paulo anapempha Akhristu kuti amupempherere. Werenganinso ndiyi.

5. Kodi Paulo anafuna kuti Akhristu apemphe chiyani kwa Mulungu pomupempherera?

______________________________

==========================================================

Kodi timapempherera malo atsopano kuti akulu athu ampingo azilalikirapo? Pa ndime ina Paulo anapempha anthu kuti amupempherere.

Aefeso 6:19:
Mundipempherere ine kuti andipatse mawu nkunditsekulira mkamwa molimbika, kuti ndizindikiritse anthu chisinsicho cha Uthenga Wabwino.

6. Kodi akulu ampingo amakhala amantha nthaŵi zina kutsekula pakamwa pawo molimba mtima?

______________________________

==========================================================

Koma sikuti ndi atsogoleri okha amene ayenera kupempherere-dwa. Werengani Aefeso 6:18, monga mmene zalembedwa pachiyambi pa phunziroli.

7. Kodi ndime iyi ikuti tizipempherera ayani? ____________

______________________________________

==========================================================

Kodi anthu a Mulungu ndi ayani? Kodi sali Akhristu amumpingo? Izi zitanthauza kuti tizipemphererana. Monga Akhristu tizipempherera anthu enanso amene amapembedza nafe pa Sabata ndi Sabata.

8. Lembani maina a Akhristu amumpingo mwanu amene muyenera kuŵapempherera.

______________________________________

______________________________________________________

==========================================================

Ngati ndinu mbusa, ndiye kuti muli ndi udindo waukulu wopempherera munthu aliyense mumpingo mwanu. Onani kuti Samueli anati m'ndime imene tinawerenga ija kuti ngati akanalephera kupempherera anthu ake, iye akanachimwa.

9. Kodi mumadziŵa kuti mtsogoleri ngati akuchimwa alephera kupempherera anthu ake?

________________

==========================================================

Koma tiyeni tikumbukire kuti si mbusa yekha amene ali ndi ntchito ya m'tchalitchi. Yakobo anati m'ndime imene tinaŵerenga ija kuti aliyense wa ife ayenera kubvomereza machimo ake kwa mnzake ndipo ndi kupempherana.

10. Kodi ndi anthu angati amumpingo amene ayenera kupempherera mpingo?

________________

==========================================================

*************************************************************

MAYANKHO.

4. Inde.
1. Pakuthokoza ndi kumlemekeza Mulungu.
10. Onse.
3. Akhristu.
5. Kuti Mulungu aŵapatse mwayi wakulalikira.
8. Kodi munalemba maina a Akhristu amene mumapita nawo ku tchalitchi? Ngati munatero ndiye kuti mwakhoza.
2. Akazi okwatiwa kapena amuna okwatira, ana, abale ndi alongo, azakhali anu, akazi a atsibweni anu, atsibweni anu, achibale, anansi, olamulira ndi adani.
7. Anthu a Mulungu.
9. Ngati zimenezi simunazidziŵe ndi kale lomwe, mwazidziŵa tsopano.
6. Inde, iwo ndi anthu monga ife tomwe ndipo nthaŵi zina amachita mantha.

SABATA LACHINAYI: KODI TIYENERA KUPEMPHERERA CHIYANI?
TSIKU LACHISANU:

Dzulo tinaphunzira za gulu la anthu amene timaiŵala kuŵapempherera nthaŵi zina.

1. Kodi ndi ayani? ______________________________

=================================================

Mpakana pano takhala tikunena za anthu amene ali pafupi nafe ndi amene amakhudza miyoyo yathu. Palinso chinthu china chimodzi chimene tiyenera kuchipempherera chimene sichili chapafupi kuchizindikira. Paulo analemba.

Aefeso 6:12:

> Chifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nawo mwazi ndi thupi, komatu tilimbana nawo maukulu, ndi maulamuliro ndi akuchita zolimbika adziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a choipa m'nzakumwamba.

Pa mawu ameneŵa Paulo amatiuza kuti Akhristu ali kumenya nkhondo.

2. Kodi nkhondoyi ndiyomenyana ndi anthu? ______________

=================================================

Iyi ndi nkhondo yosiyana ndi nkhondo zina za dziko lapansi. Iyi ndi nkhondo ya uzimu. Iyi ndi nkhondo yokangana ndi mphamvu ya Satana. Satana afuna kuti agonjetse dziko lino lapansi pamodzi ndi anthu omwe. Ife tiyenera kumenyana naye.

3. Kodi nkhondoyi tingaimenyere ndi malupanga kapena mfuti?

______________________________

=================================================

Nkhondoyi tingathe kumenyera ndi chinthu china chake chimene chili cha uzimu. Paulo amatiuza kuti tiyenera kuimenya ndi

pemphero. Atafotokoza za nkhondoyi Paulo analemba mawu amene tinawerenga dzulo.

Aefeso 6:18:

Mwa pemphero lonse ndi pembedzero mupemphere nthaŵi zonse mwa Mzimu ndipo pochezera pamenepo chichezerere ndi kupembedzera oyera mtima onse.

4. Kodi tingathe bwanji kumenya nkhondo ndi Satana?

______________________________________________

==========================================================

Mulungu amatilonjeza kuti tikamapemphera ndiye kuti tidzagonjetsa Satana.

Aroma 8:37-39:

Koma m'zonsezi, ife tilakatu, mwa Iye amene anatikonda. Pakuti ndakopeka mtima kuti ngakhale imfa, ngakhale moyo, ngakhale angelo, ngakhale maufumu, ngakhale zinthu zilipo, ngakhale zinthu zilinkudza, ngakhale zimphamvu, ngakhale utali, ngakhale kuya, ngakhale cholengedwa china chilichonse, sichingadzakhoze kutisiyanita ife ndi chikondi cha Mulungu, chimene chili mwa Khristu Yesu Ambuye wathu.

5. Kodi Satana angathe kutigonjetsa ngati tipitirizabe kupemphera?

____________________

==========================================================

Pamene Yesu anali kuphunzitsa ophunzira ake kupemphera anaŵauza kuti anene motere.

Mateyu 6:10:

Ufumu wanu udze. Kufuna kwanu kuchitidwe, monga kumwamba chomwecho pansi pano.

Ichi ndi chimene tikumenyanirana, ndipo ndicho tiyenera kuchipempherera. Tikufuna chifuniro cha Mulungu kuti chichitidwe pansi pano.

6. Kodi tiyenera kupempherera chiyani pamene tili kumenyana ndi Satana?

______________________________

==========================================================

Taonani mmene Danieli anapempherera kuti chifuniro cha Mulungu chichitidwe.

Danieli 9:2-3:

Ine Danieli ndinazindikira mwa mabuku kuti chiwerengero chake cha zaka zimene Mawu a Yehova anadzera nacho kwa Yeremiya mneneri, kunena za makwaniridwe a mapasuko a Yerusalemu, ndizo zaka makumi asanu ndi ziŵiri. Ndipo ndinaika nkhope yanga kwa Ambuye Mulungu, ndi mapembedzero. Ndikusala, ndikumfunsa Iye mu mpemphero, ndi ziguduli ndi mapulusa.

Powerenga mawu a mneneri, Danieli anaona kuti Mulungu anafuna kupulumutsa Yerusalemu patatha zaka makumi asanu ndi aŵiri (70). Danieli anaona kuti zaka makumi asanu ndi aŵiri zinatsala pang'ono kuti zithe. Kodi iye anatani? Kodi iye anangoti, "Chabwino, zikatero zili bwino. Tsopano Mulungu adzapulumutsa Yerusalemu?" Ayi, iye anayamba kupemphera kuti chifuniro chake cha Mulungu chikachitike.

7. Kodi Danieli anangoyerekeza kupemphera, kapena anapemphera ndi mtima wake wonse?

______________________________

==========================================================

Pano pali ntchito ya ife tonse yakuti tichiteko. Mulungu amafuna kuti achite zinthu m'dziko lino lapansi, koma Iye waganiza kuti adzagwira ntchito yake pokhapokha ngati ife titapemphera. Iye amafuna kuti tithandizane kumenya nkhondo yomenyana ndi Satana. Choncho Iye akutipempha ife kuti tipemphere kuti chifuniro chake chichitike.